



NDONDOMEKO YA CHIKONZERO CHOSAMALIRA BULOKO YA MSANKHILE

NKHALANGO YOSUNGIDWA YA NTCHISI



KUYAMBILA: 2013-2018

ZAMKATIMU

MAU OTHOKOZA

Tifuna kuthokoza kuchokera pansi pa mtima anthu onse amene adathandiza pa chikonzero cha ndondomeko ya Buloko ya Chisamaliro cha nkhalango kwa Msankhile. Pali a GVH Msankhile, anthu onse a m'derali, Mwinimtunda[Chalo] Nthondo, mafumu onse ndi Mamembala a Buloko ya Msankhile.

Tikuperekanso kuthokoza kwathu kwa kagulu ka akuluakulu a zankhalango a mu boma la Ntchisi awa: T. Mboma [DFO], A. J. Palani, B Munthali, M. Masimbe, G.Mpotachamba . chifukwa cha mathandizo awo osiyanasiyana pa maluso awo komanso zina zofunikira pa ntchito ya zankhalango.

Tikuthokozanso kwa kagulu ka akuluakulu a zankhalango a kuchigawo chapakati monga bambo R. W. S. Nyirenda [Mlangizi wa za luso wa Ndondomeko yotukula kasamalidwe ka nkhalango cuti pakhale kupititsa patsogolo umoyo wa anthu **IFMSLP**], T. S. Ketulo [M'thandizi wolumikiza ntchito za nkhalango m'chigawo chapakati], chifukwa cha mathandizo awo osiyanasiyana pa maluso awo komanso zina zofunikira pa ntchito ya zankhalango zimene zidafika mu nthawi yake.

Mwapadera tikuthokozanso bungwe la EU pothandiza ndi ndalamu zonse zimene zidachitika pa ntchitoyi cuti chikonzero cha chisamaliro chankhalangochi chilembewo.

Kuthokoza

MAU ACHIDULE OFUNIKA KUWADZIWA AMENE AGWIRITSIDWA NTCHITO MKATIMU

- FUG : Gulu la Mamembala ogwiritsa ntchito nkhalango
- DFO : Wamkulu wa zankhalango mu Boma [LA NTCHISI]
- T/A : Mwinimtunda – [chalo/ Gogo]
- IFMSLP : Ndondomeko yotukula kasamalidwe ka nkhalango kuti pakhale kupititsa patsogolo umoyo wa anthu.
- EU : Bungwe la azungu la ku Ulaya limene lidathandiza ndi ndalamu kuti ntchitoyi ichitike
- FMU : Gawo la kasamalidwe ka nkhalango
- LFO : Bungwe la kumudzi loona zankhalango
- FD : Nthambi ya maofesi a zankhalango [Dipamenti yoona zankhalango]
- BMC ; Bungwe Losamalira Buloko
- VH : Amfumu a m'mudzi [a Nyakwawa]
- EPA : Dera lalikulu la chionjezero pa chikonzekero cha ntchito za nkhalango

LFMB : Bungwe loyang'anira chisamaliro cha nkhalango yotetezedwa

PCU : Kagawo kolumikiza m'ndandanda wa zintchito zoyendetsera nkhalango

GVH : Mfumu yoyang'anira midzi ingapo


NGO : Bungwe Limene silaboma

VNRMC : Bungwe la m'mudzi Loyang'anira zachilengedwe

1. MAU OYAMBA

Chikonzero cha chisamaliro cha nkhalango ichi chidzalongo soledwa ndi a Bungwe la Mgirizano wa chisamaliro cha nkhalango mu Buloko ya Msankhile ndi thandizo lochokera ku Nthambi ya maofesi oona zankhalango [Dipamenti yoona zankhalango]. Pali midzi isanu [midzi 5] mwa a Gulupu Msankhile. Midziyi ndi Msankhile, Kasiteni, Kholowa, Kayera1 ndi Kayera 2 ndipo muli mabanja 92. Bungwe la Mgirizano wa chisamaliro cha nkhalango mu Buloko ya Msankhile lidzaonetsetsa kuti Chikonzero cha chisamaliro cha nkhalango chikutsatidwa.

MAPU A BULOKO YA MSANKHILE



2.0 ULAMULIRO PA CHISAMALIRO CHA NKHALANGO

Dera lalikulu lankhalango la Msankhile ndi losamalidwa ndi ogwira ntchito m'boma oona zankhalango mu Dipatimenti ya zankhalango pamodzi ndi eni dera limene lili pansi pa agulupu a Msankhile [GVH] monga mwa lamulo la zankhalango la 1997 limene limalola mgwirizano wa chisamaliro cha nkhalango zosungidwa m'dziko lino. A Gulupu Msankhile ali kum'mwera kwa T/A Nthondo. Iwowa ali ndi mafumu asanu pansi pawo amene ndi a Msankhile, Kasiteni Kholowa, Kayera 1 ndi Kayera 2.

KUFOTOKOZERA ZA NKHALANGO

3.1 KUFOTOKOZERA ZONSE MWACHIDULE

Dera lalikulu la nkhalango ya Msankhile lili pa mtunda wa 20km chakum'mawa kwa likulu la Ntchisi Boma. Buloko ya Msankhileyi ili kumadzulo kwa nkhalango yosungidwa ya Ntchisi m'dera la Gogo Nthondo mu boma la Ntchisi.

3.1.1 ZOMERA ZOSIYANASIYANA ZA MDERALI

Dera lalikulu la buloko ya Msankhile lili ndi mitundu yosiyanasiyana koma imene imapezeka mochulukirapo ndi sanga ndipo imene chiwerengero chake chimatsatira mitengo imeneyi ndi Mseza.

3.2.1 MITUNDU YA DOTHI LOSIYANASIYANA

Mitundu ya dothi lopezeka kwambiri mu Buloko ya Msankhile ndi dothi la mchenga lophatikiza ndi katondo. Derali lili ndi makwawa ndi zigwembe zoyendeka ndithu. Madera ena ali ndi mitengo yothinana pamene ena ali ndi mitengo ya apo ndi apo makamaka cha ku fupi ndi mtsinje wa Katsuka.

3.2 MALIRE

Malire a Buloko ya Msankhile idapakidwa utoto[penti]. Pali penti yofiira ndipo m'madera ena malire a Buloko ndi mtsinje. Cha ku mpoto kwa bulokoyi kuli mtsinje wa Katsuka womwe udapanga malire ndi dere la Kasakula, pamene ku mwera kuli mtsinje wa Chafumbi womwe ukupanga malire a buloko ndi mudzi wa Msankhile..

3.3 UMWINI WA MALO

Dera la Chigawo cha Buloko ya nkhalango ya Msankhile ili pansi pa ulamuliro wa boma ndi mgwirizano wosamalira limodzi ndi eni dera. Anthu onse a m'dera la Msankhile pamodzi ndi Boma la Malawi adzakhala ndi udindo woyang'anira nkhalangoyi komanso kudzapezamo phindu. Komabe umwini wa nkhalangoyi uli m'manja mwa Boma.

3.4 OGWIRITSA NTCHITO NKHALANGO

Anthu onse a dera la a GVH Msankhile ndi amene adzakhala oyambirira kudzagwiritsa ntchito zinthu zosiyanasiyana kuchokera m'nkhalango imeneyi. Midzi imene ili pansi pa ulamuliro wa agulupuwa idzakhala nazo mphamvu zovomerezera midzi ina imene siili mu dera la agulupu amenewa kuti apeze zinthu za m'nkhalango imeneyi . Pali zina zimene anthu a mu Buloko imeneyi amatenga ulele, mwachitsanzo bowa, zipatso, ndi zina. Koma izi sizikhudza iwo amene siali mu Buloko imeneyi. Kutenga kena kalikonse m'nkhalangoyi kungachitike pokhapokha pali chilolezo choperekedwa ndi Bungwe Loona za chisamaliro cha buloko [Msankhile BMC]. Izi zotenga chilolezo zikukhudza wina aliyense wa m'derali kapenanso amene sachokera m'derali.

3.5 NTCHITO ZA NKHALANGO ZAZIKULUZIKULU

Anthu onse adzaloledwa kudzapeza nkhuni ndi zinthu zina zonse zochokera m'nkhalangoyi. Phindu lochokera m'nkhalangoyi ndi zinthu monga nkhuni, matabwa, phaso, luzi, zipatso, mtera, udzu wovikira nyumba, matondo ndiponso bowa.

4.0 TIMADERA TACHISAMALIRO CHA NKHALANGO [FMUs]

Chigawo Chachikulu chosamalira zankhalango cha Msankhile [Buloko ya Msankhile] chili ndi magawo awiri a timadera tachisamaliro cha nkhalango [FMUs] motere:

FMU 1 DERA LOSAKOLOLEKA KOMA NDI MMPHEPETE MWA MITSINJE NDI MALO OTSETSELEKA


Kukula kwake ndi 272.75 ha ndipo malowa ndi otetezedwa omwe sayenera kukololedwa. Malowa ali ndi malo otsika kwambiri m'mene mumapezeka makwawa ndi zigwembe. palinso malo amene anadulidwa mitengo yonse ndi anthu akuba, kofunika kutetezedwe kuti ziphukira zikule.

FMU 2 DERA LOYENERA KUPEZAKO PHINDU


Derali lili ndi mitengo yambiri yomera mothinana ndipo ndi malo omwe ayenera kukololedwa mwa dongosolo ndi cholinga chofuna kupezamo phindu. Malo awa ndi okwanira mahekitala 200 ha. Mitengo imene ikupezeka m'derali ndi mtundu wa Miyombo.

CHITHUNZI CHA DERA LOTETEZEDWA KOMA GWERO LA MITSINJE

[FMU 1]



CHITHUNZI CHA DERA LOYENERA KUPEZAKO PHINDU [FMU 2]



4.1 ZOLINGA ZAZIKULU ZOLUNJKA KWENIKWENI MADERA OKOLOLEKA NDI OSAKOLOLEKA

Dera losakololeka

- Kuteteza anthu kuti asadule mitengo kudera limene ndi gwero la mitsinje
- Kuteteza udzu ndi zomera zobiriwira za m'mphepete mwa timitsinje ndi malo omwe ali kufupi ndi mtsinje wa Katsuka kumene kunadulidwa kwambiri kofunika kutetezedwe.

Dera Lokololeka

- Kufuna kukololamo nkhuni, matabwa, phaso zogwiritsa ntchito panyumba ndi pochita malonda ndicholinga chotukula miyoyo yathu pa chuma m'dera lonse la GVH Msankhile.
- **Kuti pakhale kutulutsa zinthu za bwino ndi za luso pa zosemasema ndi zina zonse zochokera m'nkhalango.**

4.2 ZOLINGA ZOCHEPERAPO KOMA ZOLUNJIKA KWENIKWENI DERA LOKOLOLEKA NDI LOSAKOLOLEKA

Dera losakololeka

- Kuteteza udzu ndi zomera zobiriwira za m'mphepete mwa timitsinje ndi cholinga chofuna kuti madzi aziyenda chaka chonse kuti anthu azigwiritsa ntchito pa ulimi wa mthirira ndi ntchito zina za m'makomo.
- Kuteteza nthaka imene ili malo ozyolika [opendekeka kwambiri]
- Kulimbikitsa chitetezo cha nyama za m'tchire ndi maluwa a m'thengo.

Dera Lokoleka

- Kupititsa patsogolo ntchito yotulutsa zinthu zabwino zochokera m'nkhalango kuti anthu azigwiritsa ntchito m'makomo ndi zina zokagulitsa.

5.0 ZOLINGA ZA CHISAMALIRO CHA NKHALANGO

5. 1 CHOLINGA CHACHIKULU

- Cholina chachikulu ndiko kuteteza, kupereka chisamaliro cha nkhalango pamodzi ndi eni dera lozungulira nkhalango yosungidwa ndi boma. Padzakhalanso kugwiritsa bwino ntchito zinthu zonse

zochokera m'nkhalango, mosungako zina kuti tsiku lina zidzagwirenso ntchito m'makomo kuti miyoyo ya anthu ozungulira nkhalangoyi ipite patsogolo.

- Kupititsa patsogolo chisamaliro cha phindu lonse lochokera m'nkhalango ndi miyoyo ya anthu ozungulira nkhalangoyi.

5. 2 ZOLINGA ZOCHEPERAPO KOMA ZOLUNJIKA KWENIKWENI NTCHITO YA CHISAMALIRO CHA NKHALANGO

- a) Kuteteza malo otsika kwambiri ndi malo amene ali m'mphepete mwa mitsinje kuti madzi azipezeka mosavuta nthawi zonse ngakhale kulibe mvula ndipo pakutero mitsinje idzapereka madzi chaka chonse ndipo madzi otengedwa kudzera m'mapaipi adzafikira anthu nthawi zonse mwa mphamvu.
- b) Kuti anthu apeze bwinobwino phindu pa zinthu zogulitsidwa kuchokera m'nkhalango.
- c) Kupeza zosowa zathu za tsiku ndi tsiku.
- d) Kulimbikitsa chiterezo cha nyama za m'tchire ndi maluwa a m'thengo.
- e) Kuonetsetsa kuti nyengo yabwino ndi kagwedwe ka mvula kasasinthe m'derali ndipo pakutero ulimi upitirire.
- f) Kuonetsetsa kuti mitundu ya mitengo yosiyanasiyana ikusungidwa ndi kulimbikitsa kumeretsa mitundu ya mitengo yatsopano ndi imene ilipo m'njira ya mbalame

ndi nyama zimene zimatenga njere ndi kukazitaya kwina kumene zimamera.

g) Kuteteza kukokoloka kwa nthaka m,malo otsetsereka ndi m,mphepete mwa mitsinje.

h) Kuperekala okhalamo nyama za m'thengo.

i) Kulimbikitsa ntchito zokopa alendo zimene zimabweretsa ndalama ku dziko.

6. MALAMULO A KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA ZINTHU ZA MNKHALANGO

Malamulo awa akukhudza Buloko ya Chifwerekete yonse

NO.	Malamulo okhudza mitengo ndi zina zochokera m'nhalango	Kufotokozer ntchito yogwirika ndi Bungwe La Chigawo Chachikulu Loyang'anira za Nkhalango ya Msankhile BMC	Zilango
1)	Kudula mitengo m'nhalangoyi opanda chilolezo nkoletsedwa	Ntchito yodula nkhuni, mitengo ya matabwa, phaso m'nhalangoyi adzayang'anira ndi a Bungwe la	Aliyense wopezekwa akudula mitengo opanda chilolezo

		<p>Msankhile BMC komanso ogwira ntchito ku nthambi ya maofesi a zankhalango [Dipatimenti yoona zankhalango]</p>	<p>adzalipira chinapusa cha K2000 kapena nkhuku ziwiri.</p>
2)	<p>Aliyense wokana kutengapo gawo mu ntchito zosiyanasiyana mu dera la GVH Msankhile pa chisamaliro cha nkhlangoyi adzapatsidwa chilango</p>	<p>Ntchito zonse zidzayang'aniridwa ndi Bungwe la Msankhile BMC komanso ogwira ntchito ku nthambi ya maofesi a zankhalango [Dipatimenti yoona zankhalango]</p>	<p>Aliyense wopezekwa wolakwa chifukwa chokana kutenga nawo gawo pa zintchito adzalipira K1,000.00 pa tsiku lililonse</p>
3)	<p>Kuyatsa moto opanda chilolezo mu nkhlangoyi mu Buloko ya Mpamila nkoletsedwa</p>	<p>Ogwira ntchito ku nthambi ya maofesi a zankhalango [Dipatimenti yoona zankhalango] adzaonetsetsa kuti nkhlangoyi ikulambulilidwa pa</p>	<p>Aliyense wopezekwa akuyatsa moto wopanda chilolezo adzalipira chinapusa cha K15000 kapena nkhuku 15.</p>

		<p>nthawi yake, kutenthera moyambirira, kuiteteza ku moto wolusa</p>	
4)	<p>Palibe wololedwa kumanga nyumba kapena kulima mu nkhalango ya Buloko ya Msankhile</p>	<p>Ndi wamkulu woona zankhalango yekha m'Malawi amene angavomereze kumanga kanthu m'nkhalangoyi</p>	<p>Aliyense wopezeka wolakwa chifukwa chomanga china chili chonse kapena kulima m'nkhalangoyi adzalipira K10,000 kapena nkhuku 10</p>
5)	<p>Kusintha malire a nkhalango mu Buloko ya Msankhile nkoletsedwa</p>	<p>Bungwe la Msankhile BMC kawirikawiri lidzaonetsetsa kuti malire akutsatidwa</p>	<p>Aliyense wopezeka wolakwa chifukwa chosintha malire a nkhalangoyi adzalipira chinapusa chokwana</p>

			K100,000.00
6)	<p>Kudyetsa ziweto mu nkhalango ya Buloko ya Msankhile kudzayenera kulolezedwa ndi Bungwe la kumudzi la zankhalango. Chilolezo ndi K1,000 pa ng'ombe imodzi pa chaka.</p>	<p>Kudyetsa ziweto kudzafunika kuti kukhale kwa kasinthasinthia</p>	Aliyense wopezekwa wolakwa chifukwa chodyetsa ziweto m'nkhalangoyi opanda chilolezo adzalipira chinapusa chokwana K250. Pa ng'ombe imodzi.
	<p>Palibe amene ali wololedwa kutchera misampha nyama za m'thengo m'nkhalangoyi</p>	<p>Bungwe la Mpamila BMC, anthu onse a derali ndi ogwira ntchito zoona nkhalango adzaonetsetsa kuti pali kuyendera nkhalangoyi nthawi zonse</p>	Aliyense wopezekwa wolakwa chifukwa cha kutchera misampha nyama zam'thengo m'nkhalangoyi adzalipira chinapusa cha K100,000.00

7)	Palibe wololedwa kukasaka nyama mu buloko ya Msankhile	Bungwe la Msankhile BMC, anthu onse a derali ndi ogwira ntchito zonna nkhalango adzaonetsetsa kuti pali kuyendera nkhalangoyi nthawi zonse	Aliyense wopezekwa wolakwa chifukwa chosaka nyama m'nkhalangoyi adzalipira chinapusa cha K50,000.00
8)	Kuotcha makala nkoletsedwa	Bungwe la Mpamila BMC, anthu onse a derali ndi ogwira ntchito zonna nkhalango adzaonetsetsa kuti pali kuyendera nkhalangoyi nthawi zonse	Aliyense wopezekwa wolakwa chifukwa chootcha makala m'nkhalangoyi adzalipira chinapusa cha K1,000.00

7.0 MFUNDO ZOTSATIRA PAKASAMALIDWE KA NKHALANGO MU DERA LA MPAMILA

7.1 CHIKONZERO CHA KAGWIRIDWE KA NTCHITOYI

Ntchito zalembedwa m'munsizi zizidzagwirika chaka chilichonse.

No.	NTCHITO	ZOFUNIKIRA	KODI	M	J	F	M	A	M	J	J	A	S	O	N	Dec
			NDI	A	a	e	ar	p	a	n	u	l	e	e	ct	o
1.	Ntchito yoperek a zilolezo zokazulir a [zokatol era] bowa	Zolemb era ndi Buku la zilolezo	Bung we la Mpa mila BMC	B	✓	✓	✓	✓								
2.	Kutenth a	Makeni ndi	Bung we la	B									✓	✓		

	moyam birira kutetez a nkhalan go kuti isapsye ndi moto wolusa	moto	Mpa mila BMC ndi anthu onse m'der ali	I o k o y a M p a m il a										
3.	Kukonza nso[kula mbura] njira zozimira mo moto wolusa kuzungu lira nkhalan go	Zikwanj	Bung e, makasu ndi nkhwan gwa	B we la Mpa mila BMC ndi anthu onse m'der ali	✓ U I o K o y a M p a	✓	✓							

				m il a									
4.	Kudula malire a timader a tating'o noting'o no tolimam o	Zolemb era, GPS ndi Buku Iolemb amo za konse kumene kwayen deredw a	Bung we la Mpa mila BMC ndi ogwir a ntchit o za nkhal ango	B U I O K O y a M p a m il a			✓	✓	✓	✓	✓	✓	

5.	Kuika Zizindikir o za mitengo yofunika kusunga	Penti, zotchet chera, mabula shi, zolemb era ndi mapep ala ndi zina zofunik a polemb a	Bung we la Mpa mila BMC ndi ogwir a ntchit o za nkhal ango a	B U I O K O Y A M P A M I A	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓
6.	Kukolola mitengo m'nkhal ango	Nkhwa ngwa, pentí, Zikwanj e, mipeni yochek era matab wa[mp	Bung we la Mpa mila BMC ndi ogwir a ntchit o za nkhal	B U I O K O Y A M	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓

		eni wauta – sowo ndi mpeni waukul U	ango	p a m il a																			
7.	Kuyend era Nkhalan go	Zolemb era, zotchet chera, Buku Iolemb amo zochitik a ndi zopeze ka poyend era nkhalan go ndi buku Iolemb	Bung we la Mpa mila BMC ndi ogwir a ntchit o za nkhala ango	B u l o k o y a M p a m il o	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓

		amo za konse kumene kwayen deredw a																							
8.	Kuperek a zilolezo za katundu wosiyan asiyana wochok era m'nhal ango	zolemb era ndi mapep ala ndi zina zofunik a polemb a	Bung we la Mpa mila BMC ndi Wam kulu woon a za nkhal ango m'Ma lawi[DFO] ngati zinthu zake ndi zokag	B U I O K O y a M p a m il a	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	

			ulitsa												
9.	Kuchita kafukuf uku wa misika ya malond a osiyana siyana	zolemb era ndi mapep ala ndi zina zofunik a polemb a komans o ndalam a	Gulu la Mam emba la ogwiri tsa ntchit o nkhal ango[FUG] ndi ogwir a ntchit o za nkhal ango	B U I O K O M Y A P A M I A O	✓										
10.	Kugulits a phindu losiyana siyana lochoke	zolemb era ndi mapep ala ndi zina zofunik	Bung we la Mpa mila BMC , ogwir	B U I O K O	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	✓	

ra	a	a	y									
m'nhal	olemb	ntchit										
ango	a	o za	a									
		komans	nkhal									
	o	ango	M									
	mabuk	ndi	p									
	u a	onse	a									
	malisiti	okhal	m									
		a	il									
		m'der	a									
		ali										

7.2 NDONDOMEKO YA M'MENE ANTHU AKHOZA KULONDERA NKHALANGO

Kulondera nkhalango kudzachitika Kawiri pa sabata ndipo anthu ochokera ku midzi yotsatirayi adzatengapo gawo pa ntchito imeneyi pamodzi ndi ogwira ntchito ku Dipatimenti yoona za nkhalango. Midziyi ndi iyi:

Mpamila 1, Mpamila 2, Ndale Ndaule, Ngoza, Disoni, Ngoza Siwande, Matamula, Mateche 1, Mateche 2, Mkoza, Chimbalanga 1, Chimbalanga 2, Jakeseni, Kango, Funsani, M'bwerachaje, Odala, Chigalu, Kambale, Jimu, Maluza, Kapakasa, Zimbwe, ndi Kawiya.

NTCHITO	KODI ADZAGWIRE NTCHITIYO NDANI?	KODI IDZAGWIRIKA KANGATI PA SABATA IMODZI?	ZIZINDIKIRO ZOSONYEZA KUTI NTCHITO YAGWIRIKA
Kuletsa kugwetsa mitengo kwa iwo amene alibe chilolezo	Bungwe la Mpamila BMC ndi ogwira ntchito za nkhalango ku ofesi ya boma	Kanayi pa sabata	Kuchuluka kwa matabwa amene alandidwa, Kuchuluka kwa mitengo imene yagwetsedwa, kuchuluka kwa zida zimene zalandidwa
Kuletsa okumba mbuna[maenje a misampha yogweramo nyama akazitchera]	Bungwe la Mpamila BMC ndi ogwira ntchito za nkhalango	Kamodzi pa sabata	Kuchuluka kwa zida zimene zalandidwa, Kuchuluka kwa milandu,

	ku ofesi ya boma		Kuchuluka kwa olakwira ndi kuchuluka kwa mbuna
Kuletsa ocheka matabwa kwa iwo amene alibe chilolezo	Bungwe la Mpamila BMC ndi ogwira ntchito za nkhalango ku ofesi ya boma	Kanayi pa sabata	Kuchuluka kwa zida zimene zalandidwa, kuchuluka kwa matabwa amene alandidwa, Kuchuluka kwa olakwira, Kuchuluka kwa mitengo imene yagwetsedwa ndi Kuchuluka kwa milandu imene yalembedwa m'buku,
Kuletsa kuyatsa moto mwachisawawa	Bungwe la Mpamila BMC ndi	Kamodzi pa sabata	Kuchuluka kwa milandu, kuchuluka

[mosatsata dongosolo lotenthera dera la nkhalango kuiteteza ku moto wolusa]	ogwira ntchito za nkhalango ku ofesi ya boma		kwa zida zimene zalandidwa
Kuletsa osaka nyama za m'tchire kwa iwo amene alibe chilolezo	Bungwe la Mpamila BMC ndi ogwira ntchito za nkhalango ku ofesi ya boma	Kawiri pa sabata	Kuchuluka kwa olakwira, Kuchuluka kwa milandu ndi kuchuluka kwa zida zimene zalandidwa

**7. 3 KAUNIUNI [KALONDOLONDO] WA NDONDOMEKO
ZOKHAZIKITSIDWA KUTI ZITSATIDWE MONGA MWA
CHIKONZERO PANTCHITOYI**

Cholina	Zofunika kuyesed wa	Kuyesa kwake	Zizindikiro zake zosonyez a kuti ntchito yogwirika kapena	Kodi ndi Udindo wa ndani	Nthawi yake yogwira ntchitoyi [Miyezi]
----------------	----------------------------------	------------------------	--	---------------------------------------	---

			ayi		
Kukonza njira zoletsa moto wachisa wawa kutentha nkhala ng o	Mtunda umene njira yakonze dwa	Kupitak o kumalo ko, kuzukut a[kuya ng'anit sitsa bwinob wino ndi malipot i	Chiweren gero cha mtunda wa njira zakonzed wa Kuletsa moto wachisaw awa	Bungwe la Mpanan g'ombe BMC ndi Ogwira ntchito a boma a zankhala ngo	May mpaka June
Kutentha moyambi ria kuteteza nkhala ng o kuti isapsye ndi moto wolusa	Chiweren gero cha dera limene latenthe dwa	Kupitak o kumalo ko ndi kuzukut a[kuya ng'anit sitsa bwinob	Kukula kwa dera limene lidatenth edwa mwansan ga kuteteza nkhala ng o ku moto	Bungwe la Mpamila BMC ndi Ogwira ntchito a boma mu ofesi ya zankhala	Sept mpaka Oct.

		wino	wolusa	ngo	
Kukolola phindu losachok era ku mitengo	Kuchuluk a kwa phindu lililonse kupatula wochoke ra ku mitengo	Kuwere nga, kuchul uka kwa zilolezo ndi kuzukut a[kuya ng'anit sitsa]	Mtolo wa udzu wosenzek a pa mutu, kuchuluk a kwa bowa wozulidw a wotenge dwa mu dengu	Bungwe la Mpamila BMC ndi Ogwira ntchito a boma mu ofesi ya zankhala ngo	Chaka chonse
Kuteteza mitengo ndi nthaka ku madera onse amene ndi magwero a mitsinje kuzungulir	Kuyenda kwa madzi m'mitsinj e chaka chonse	Kupan ga maulen do okayen dera nkhala ngoyi	Mlingo wa pamene madzi alekezera mu nthaka komanso kuuma kwa madzi kooneker	Bungwe la Mpamila BMC ndi Ogwira ntchito a boma mu ofesi ya zankhala ngo	Chaka chonse

a derali			atu ndi maso kosonyez a kusowa kwa madzi m'mapai pi		
Kuyender a nkhlang oyo	Mtunda umene munthu angayen dere nkhlang oyo	Kuchul uka kwa maulen do oyend era nkhala ngoyi ndi malipot i	Chiweren gero cha milandu imene yopezeka poyender a nkhlang oyi komanso anthu amene agwidwa kapena ena amene adzapere ka	Bungwe la Mpamila BMC ndi Ogwira ntchito a boma mu ofesi ya zankhala ngo	Chaka chonse

			malipoti		
Kukonza malo ofesa mbande za mitengo[nazale za mitengo] ndi kubzyala			Bungwe la Mpamila BMC ndi Ogwira ntchito a boma mu ofesi ya zankhala ngo	April mpaka Sept.	

CHISAMALIRO CHA NKHALANGO KU DERA LOKOLOLEKA [FMU 3]

Kukolola m'dera la Mpamila BMC kudzachitika m'derali ndipo phindu lalikulu ndi nkhuni. Mitengo ya Sanga ndi imene imapezeka kwambiri m'derali. Mitundu ina ya mitengo m'derali imene anthu akhoza kugwiritsa ntchito ndi Mombo, Kamphoni, Chiyere, Mtondo, ndi Misuku.

Dongosolo la kasinthasinta amene ayenera kukhalapo mu Sanga ndi zaka 21[makumi awiri ndi mphambu imodzi] ngati mitengoyi ndi yambiri. Nthawi yotereyi idasankhidwa kuti pakhale mpata wokwanira kuti mitengo iphukirenso ndipo pakutero anthu sasowa mathandizo ochokera m'nkhalangomo ngakhale masiku azipitabe mtsogolo mpaka atakwaniritsa

kugwiritsa ntchito dera lokwanira 189.20.ha. Izi zitanthauza kuti malo okololeka ndi 9.0ha pa chaka.

8. NDONDOMEKO YA CHIKONZERO CHA KAYENDETSEDWE KA PHINDU LILILONSE LOCHOKERA M'NKHALANGO

8.1 NDONDOMEKO YA CHIKONZERO CHA CHISAMALIRO CHA NKHUNI

- a) Phindu lochokera m'nkhalango ndi nkhuni [lchi ndi chofunikira kwambiri]
- b) Mitundu ya mitengo yofunika kwambiri ndi Sanga ndi Mfukusa
- c) Imafunikira motani mitengo? Imafunika kwambiri.
- d) Mitengo imapezeka motani? Imapezeka kwambiri.
- e) Zovuta zake ndi kubedwa kwa nkhuni komanso moto wolusa zimene zimaononga nkhuni.
- f) **Chisamaliro cha nkhalango**
 - o Kugawa timadera tolimamo kudzachitika chaka chilichonse.
 - o Kutalika kwa zitsa zoosiidwa atadula mtengo ndi kokwanira 15cm kuchokera pa dothi.
 - o Kukololamo mitengo m'timadera tating'onoting'ono kudzachitika pakapita za 21 zilizonse mwakasinthasinha.

- o Kadera kalikonse kadzakhala ndi mitengo 140 yosiidwa osadulidwa.
- o Kukolola kudzachitika kuyambira April mpaka November.
- o Kulambula njira zozungulira nkhalango ntchito imene idzasiyanitsa nkhalango ku malo a anthu. Izi zikachitika kutenthera nkhalango mwansanga kuzichitika chaka chilichonse kuopetsa madera okololeka ndi ena a nkhalango ku moto wolusa chaka.
- o Timitengo tizidulidwa pa phata palii ponse kusiyapo timitengo tiwiri kuti tikule pakapita zaka ziwiri zilizonse chikololeleni.

g) Dera lololedwa kukolola chaka chilichonse

Dera lololedwa kukololako mitengo ndi 9ha pa chaka potengera kasinthasinha wa zaka 21 zili zonse wa dera lonse lokololeka lokwanira 189.2ha.

h) **ZILOLEZO**

Midzi yonse ya m'dera la Mpamila ndi yololedwa kupeza phindu kuchokera m'nkhalango ngati chilolezo chaperekedwa ndi Bungwe loyang'anira chisamaliro cha nkhalango la Mpamila BMC.

i) NDALAMA ZOLIPIRA PA ZINTHU ZOCHOKA M'NKHALANGO

- **Mtolo umodzi wa nkhuni wosenzeka pa mutu udzagulitsidwa pa K50.00 pamene anthu ena ochokera kunja kwa BMC ya Mpamila adzalipira K200.00**
-
- **Phaso** ndi nsichi lidzagulitsidwa pa K50.00 pamene anthu ena ochokera kunja kwa BMC ya Mpamila adzalipira K70.00.
- **Mtengo uliwonse wa matabwa udzagulitsidwa** pa K5,000.00 ndipo ena a kunja kwa derali adzagula pa K8,500.00.

8.1 Chithunzi chowonetsa dera lokatola nkhuni m'nkhalango.

8.2.1 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA MITENGO YA MATABWA

- a) Phindu lochokera m'nkhalango ndi matabwa [Ichi ndi chofunikira kwambiri]
- b) Mitundu ya mitengo ya matabwa yofunika kwambiri kugwiritsa ntchito ndi monga iyi: Chiyere, Mseza, Mfukusa, Sanga, M'bawa, Msikidzi ndi Mpasa.
- c) Imafunikira motani mitengo ya matabwa? Imafunika kwambiri komanso kugwiritsa ntchito ngati nkhuni zosonkhera moto.

d) Mitengo ya matabwa imapezeka motani? Imapezeka kwambiri komanso kugwiritsa ntchito ngati nkuni zosonkhera moto.

e) Zovuta zake za mitengo ya matabwa ndi njira zosayenera zokololela komanso moto wolusa woponyedwa mochedwa.

f) **Chisamaliro cha mitengo ya matabwa m'nkhalango**

- Kuika Zizindikiro timadera tonse timene tikufunika kuti tikoledwe chaka chilichonse
- Mitengo ya matabwa okagulitsa idzayenera kudulidwa ku timadera tokhato tokidwa Zizindikiro
- Mitengoyi idzadulidwa ndi kusiidwa zitsa zotalika 30cm kuchokera pansi.
- Kudula mitengo ya matabwa kudzachitika motsatira dongosolo losankhako timadera toyenera kudulako mitengoyi osati mwachisawawa.

g) **Dera lololedwa kudulako mitengo ya matabwa pa chaka**

Dera lololedwa kudulako mitengo ya matabwa ndi 6ha pa chaka motsatira kasinthasinha wa zaka 15 zilizonse mu dera lokololeka la ma hekitala zana [100ha]

h) **CHILOLEZO CHA MITENGO YA MATABWA**

- Onse olowa m'nhalango kukafuna ndi kukapeza mitengo ya matabwa ndi woyenera kutero ngati atapeza chilolezo kuchokera ku Mpamila BMC.

**i) NDALAMA ZOLIPIRA PA MITENGO YA
MATABWAYODULIDWA M'NKHALANGO**

Gome lili m'munsili likuonetsa mitengo ya phindu losiyanasiyana lochokera m'nhalango. Mitengo ya zinthuyi ndi yosiyana ndi ya midzi ina imene siili mu dera la GVH Mpamila.

Mtengo wa katundu	Anthu Ochokera kwa a Gulupu Mpamila	Mtengo wogulira katundu kwa anthu ochokera ku madera ena
Ndawala, Phaso ndi Nsichi zazing'onozing'ono		K50 K100
Phaso ndi Nsichi zazing'onozing'ono		K70 K150

8.3 Chithunzithunzi chowonetsa dera lopezako nkhuni/ndawala, phaso ndi nsichi komanso mitengo ya matabwa

8.4 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA MANKHWALA A ZITSAMBA

- a) Phindu lochokera m'nkhalango ndi mankhwala azitsamba
- b) Mitundu ya mankhwala azitsamba yofunika kwambiri ndi monga Katunga, Kalumbaanamwali, Mbundu, Mwaye, Khumbu, Chipulumbudzi, Msolo, Katope, Msambbamfumu, Mtsiloti, Sanga, Mkulansinga masoang'ombe, Kadale, Mpsyimpsy, Nthupa, Katsitsimnzukwa, M'bwazi, M'bwabwa ndi Nkhunga.
- c) Imafunikira motani mitengoyi? Imafunika chikatikati.
- d) Mitengoyi imapezeka motani? Imapezeka kwambiri.
- e) Zovuta zake za ndi kusowa kwa mitundu ina ya mitengo ya mankhwala a zitsamba yofunikirayi, kudula mitengoyi mosasamala komanso moto wolusa m'nkhalango woyatsidwa mochedwerapo umene umaletsa kuphukiranso kwa mitengo ya zitsambazi.
- f) **Chisamaliro cha mitengo ya mankhwala a zitsamba**
- Aliyense wokafuna mankhwala a zitsamba m'nkhalango ayenera kupeza chilolezo kuchokera ku Buloko ya Mpamila asanalowe m'nkhalango.
 - Aliyense wopeza chilolezo chokakumbira mitengo ya mankhwala ayenera kufotsera dzenje atakumba mankhwalawo.
 - Kumene mitengo ya zitsamba ikuphukiranso idzayenera kutetezedwa ku moto wolusa.

**g) MALO A NKHALANGO OOLEZEDWA KUPEZAKO
MANKHWALA A ZITSAMBA PA CHAKA**

Mankhwala adzakumbidwa chaka chonse mu dera la Buloko ya Mpamila ngati malamulo a zankhalango adzakhala akutsatidwa.

**h) CHILOLEZO CHOKAKUMBA MANKHWALA A ZITSAMBA
M'NKHALANGO**

- Aliyense wofuna kukakumba mankhwala a zitsamba m'nkhalango imeneyi ndi oyenera kutero bolani ngati ali ndi chilolezo cholembedwa ndi Bungwe loona za chisamaliro cha nkhalango la Mpamila BMC.

**i) NDALAMA ZOLIPIRA PA MANKHWALA A ZITSAMBA
M'NKHALANGOYI**

Mtengo wa thumba lokwanira 50kg lodzala ndi mankhwala azitsamba udzakhala K50 kwa aliyense wochokera mwa GVH Mpamila p [amene ena onse adzalipira K200 pa thumba.

8.4 Chithunzithunzi cha madera opezako mitengo ya mankhwala a zitsamba

**8.5 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA NSUNGWI
M'NKHALANGOYI**

- Phindu lochokera m'nkhalango ndi nsungwi.
- Mitundu ya nsungwi zofunika kwambiri ndi monga Biza.
- Zimafunikira motani nsungwizi? Zimafunika kwambiri.

d) Nsungwi Zimapezeka motani? Zimapezeka chikatikati osati zambiri.

e) Zovuta zake za nsungwizi ndi kubedwa komanso moto wolusa.

f) **Chisamaliro cha** nsungwi m'nkhalangoyi

- Pafunika kudula kwambiri nsungwizi kufika polekezera
- Nsungiwizi ziyenera kudulidwa ndi kusiya ziputu zotalika kulekeza 10cm kuchokera pansi.

g) **Dera limene kungapezeke nsungwi mu buloko ya Mpamila.**

Nsungwi zololedwa kudulidwa pa chaka: Kudula nsungwi m'dera lonse ndi kwa chaka chonse.

h) **CHILOLEZO CHA OKADULA NSUNGWI M'NKHALANGO**

- Aliyense wofuna kukadula nsungwi m'nkhalangoyi ndi woyenera kutero bolani atatenga chilolezo chake ku Bungwe loona za nkhalango la Mpamila BMC.

i) **NDALAMA ZOLIPIRA PA NSUNGWI ZOKADULIDWA M'NKHALANGOYI**

- Mtengo ake wa nsungwi imodzi ndi K20.00.

8.5 Chithunzithunzi chowonetsa dera lopezako nsungwi[Mapu]

8.6 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA BOWA WOCHOKERA M'NKHALANGO

- a) Phindu lochokera m'nkhalango ndi bowa
- b) Mitundu ya bowa yofunika kwambiri ndi monga iyi:
Kabwalo, Manda, Katelera, Manyame, Chipindi, Utali, Itali,
Kanamsenjere ndi Mathwe.
- c) Umafunikira motani bowawu? Umafunika kwambiri.
- d) Bowawu umapezeka motani? Umapezeka kwambiri
nthawi yamvula [Dzinja].
- e) Zovuta zake bowawu ndiko kuti umabedwa**
- f) **Chisamaliro cha bowa**
 - o Pamene anthu atengulira mitengo imene ili ndi ubale
ndi bowa mitengo yotereyi ayisiye osadula.
 - o Mitengo imene ili ndi masamba komanso masinde oola
m'maonekedwe iyenera kusiidwa kuti iwole.

- Aliyense ayenera kutenga chilolezo kuchokera ku Bungwe La Chigawo Chachikulu Losamalira za Nkhalango [BMC] asananyamuke kukatola bowa ndipo kutola bowa ndi ulele koma anthu ochokera kunja kwa Buloko ya Mpamila BMC adzalipira K200 pa ndowa imodzi.

g) Dera limene kungapezeke bowa.

- **Bowa ukhoza kutoledwa dera lonse la nkhalango ya Buloko ya Mpamila.**

h) BOWA WOLOLEDWA KUZULIDWA PA CHAKA

- Kuchuluka kwake kwa bowa woledwa kuzula m'nkhalango kudzatengera m'mene ukuperekera bowawo.
- Aliyense amene atenga chilolezo chokatolera bowa akhoza kutola bowawo m'mene angafunire.

i) CHILOLEZO CHA OKAZULA BOWA KUNKHALANGO

- Aliyense wofuna kuzula bowa m'nkhalango ndi woyenera kutero bolani atatenga chilolezo chake ku Bungwe loona za nkhalango la Mpamila BMC.

j) NDALAMA ZOLIPIRA PA BOWA WOZULIDWA M'NKHALANGOYI

Aliyense wofuna kuzula bowa m'nkhalango ndi woyenera kulipira K20.00 pamene ena onse ochokera kunja kwa dera la Mpamila adzayenera kulipira K50.00

8.6 Chithunzithunzi cha madera a nkhalango ozulako bowa.

8.7 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA ZIPATSO

- a) Phindu lochokera m'nkhalango ndi mitengo ya zipatso
- b) Mitundu ya zipatso yofunika kwambiri ndi Masuku.
- c) Imafunikira motani mitengoyi? Imafunika kwambiri.
- d) Mitengoyi imapezeka motani? Imapezeka kwambiri.
- e) Zovuta zake ndi kuthyola zipatso zosapsya, kubedwa ndi moto wolusa m'nkhalangoyi.
- f) **Chisamaliro cha Zipatso**
 - Kuthyola zipatso mokwapula zipatsozi mumtengo nkoletsedwa
 - Chisamaliro chokwanira ndi chofunikira pa mitundu ya zipatso zimene zimakula mokwawa kuti pakhale chionjezero cha zipatso.
 - Chisamaliro cha mitengo ya zipatso kuopetsa moto
 - Munthu aliyense ayenera kutenga chilolezo.
 - Kudula mitengo ya zipatso mwachisawawa ndi mosasamala nkoletsedwa

g) MALO A NKHALANGO OLOLEZEDWA KUPEZAKO ZIPATSO PA CHAKA

Zipatso zidzathyoledwa ndi kutoledwa mwa ulele chaka chonse m'nkhalango bolani ngati munthu atenga chilolezo kuchokera ku Mpamilia BMC.

h) CHILOLEZO

- Zipatso zidzathyoledwa kapena kutoledwa m'nhalango osalipira bolani ngati atenga chilolezo cholembedwa ndi Bungwe loona za chisamaliro cha nhalango la Mpamila BMC.

i) NDALAMA ZOLIPIRA PA ZIPATSO ZOCHOKA

M'NKHALANGOYI

Munthu aliyense sadzalipira kalikonse chifukwa chokathyola zipatso m'nhalango koma adera lina adzalipira K250 pa ndowa imodzi.

8.7 Chithunzithunzi cha madera a nhalango othyolako zipatso.

8.8 NDONDOMEKO YA CHISAMALIRO CHA MITENGO YA LUZI

- a) Phindu lochokera m'nhalango ndi lusi
- b) Mitundu ya lusi yofunika kwambiri ndi Sanga, Mombo, ndi Mnyangale
- c) Lusi limafunikira motani? Limafunika chikatikati osati kwambiri.
- d) Limapezeka motani? Limapezeka kwambiri.

e) Zovuta zake lusi limapezedwa m'njira yosasamala zachilengedwe ndi kuba

f) Chisamaliro cha mitengo ya lusi

- Onse ofuna mitengo ya luzi m'nkhalangoyi ayenera kutenga chilolezo kuchokera ku Bungwe loona za chisamaliro cha nkhalango la Mpamila BMC] asanakafune luzi ku nkhalango.
- Luzi lidzatengedwa pokhapokha mwadula mitengo monga ya ndawala, phaso, nsichi ndi ina imene ndi mitengo yomenyako luzi osati kungopitira kukasenda luzi ayi.
- Madera amene mitengo ikuphukiranso atetezedwe ku moto wowononga mitundu ya mitengo imene imapota pokula.

g) KUKULA KWA DERA LOSENDA LUZI M'NKHALANGO PA CHAKA

Luzi lidzasendedwa m'dera lonse la Mpamila BMC bolani ngati malamulo a Bungwe la Mpamila BMC akutsatidwa.

h) CHILOLEZO CHA LUZI LA KUNKHALANGO

Aliyense ndi woyenera kupeza chilolezo kuchokera ku Bungwe la Mpamila BMC.

i) NDALAMA ZOLIPIRA KUSENDA LUZI M'NKHALANGOYI

Aliyense wochokera kwa a GVH Mpamila adzalipira K50 pa mipukutu itatu ya luzi [nkhata zitatu za luzi].

8.8 Chithunzithunzi [Mapu] cha dera lokasendako luzi.

9 CHIKONZERO CHA KUGAWANA KWA PHINDU LOCHOKERA MU ZINTHU ZA M'NKHALANGO.

Ndalama zonse zopezeka mu zogulitsa za m'nkhalango zidzagawidwa motere:

- Ndalama zotolera ku zinthu zogulitsa zochokera m'nkhalango kuti zikagwire ntchito pakhomo zidzapite ku thumba la ndalama la Mpamila BMC.
- Ndalama zotolera ku zinthu zogulitsa zochokera m'nkhalango kuti akapeze nazo ndalama pakhomo zidzagawidwa motere:
 - 60% ya ndalamazo idzapita ku thumba la ndalama la Mpamila BMC.
 - 30% ya ndalamazo idzapita ku Dipatimenti yoona zankhalango ya m'boma la Ntchisi.
 - 10% ya ndalamazo idzapita ku Bungwe loyang'anira chisamaliro cha nkhalango la LFMB.

Katundu yense wochokera m'nkhalango adzagulitsidwa ndi kulandira ndalama zenizeni ndi kuperekira malisiti ake enieni kwa wogulayo pompopompo.

9.1 NDALAMA ZOTOLERA KUCHOKERA MADERA OSIYANASIYANA

Mlingo	Gulu	Dzina	Osainira	Ntchito za ndalama	Ndemanga
wa	lake la	la			
kochok	Ndalam	bank			
era	a	i			
ndalam	zotolera	imen			
a		e			
zotolera		idats			
		ekuli			
		dwa			
Thumba	Ndalam	Akau	Mamemb	• 40%	• Ndalama
la	a	nti ya	ala	ndalam	zonse [100%]
Ndalam	zotolera	Bung	osankhidw	a	zotoleredwa
a	kuchok	we a	a	zoyende	ku misonkho ya
zochok	era ku	Mpa	Bungwe la	tsera	zinthu
era ku	zilolezo	mila	Mpamilia	ntchito	zokagwira
phindu	pa	BMC	BMC	za	ntchito
la	zinthu	Loya	loyang'ani	chisamal	m'makomo
Nkhalan	za	ng'a	ra za	iro cha	zidzaikidwa mu
go	ntchito	nira	Nkhalang	nkhalan	akaunti
yosungi	za	za	o	go.	imeneyi
dwa	m'mako	Nkha		• 30%	• Phindu
	mo	lang		Ndalam	lochokera ku
		o		a	zilolezo
				zoyende	zoperekedwa
				tsera	nai a Bungwe
				chitukuk	la Mpamilia

				<p>o cha m'dera</p> <ul style="list-style-type: none"> • 20% <p>ndalam a zogwira ntchito zadzidzi dzi.</p> <ul style="list-style-type: none"> • 10% <p>Ndalam a zomabw ereketsa [za ngongol e]</p>	BMC
Ndalam a zochok era ku phindu la Nkhalan go yosungi	Ndalam a zotolera kuchok era ku zilolezo pa zinthu zokaguli	Thum ba la ndal ama la Bung we a Mpa mila	Mamemb ala osankhidw a Bungwe la Mpamila BMC loyang'ani ra za	<ul style="list-style-type: none"> • 40% <p>ndalam a zoyende tsera ntchito za chisamal iro cha</p> <ul style="list-style-type: none"> • 60% ya ndalama zotolera zidzaikidwa ku thumba la Mpamila BMC • Magawo atatu mwa magawo khumi [30%] a 	

dwa	tsa	BMC Loya ng'a nira za Nkha lang o	Nkhalang o ndiponso ovomerez edwa ndi Wamkulu woona zankhalan go pa boma [DFO]	nkhalan go. • 30% Ndalam a zimene adzagwi ritsa ntchito ndi a VDC. • 10% Ndalam a zimenezi adzagwi ritsa ntchito	ndalama zotolera pa misonkho ya zochokera m'nkhalango zidzaikidwa mu akaunti ya chitukuko cha nkhalango[FDF]] • Gawo limodzi la magawo khumi la ndalamazo [10%] lidzaikidwa ku thumba la oyendetsa za nkhalango ya kumudzi[LFMB]
-----	-----	--	--	---	--

9. MFUNDO ZOKHUDZA NDALAMA

Bungwe a Mpamilia BMC Loyang'anira za Nkhalango likuyembekezekwa kudzapereka zilolezo zosiyanasiyana pa

phindu la zinthu zochokera m'nkhalango pa mitengo yosiyanasiyana molingana ndi m'mene ilili ntchito yake kukagulitsa zinthu kapena kukagwiritsa ntchito pakhomo. Mitengo ya Zilolezo potolera ndalama za m'nkhalango pa zinthu zokagulitsa ndi zokagwiritsa ntchito pakhomo idabwera poganzira mfundo zimene zidaperekedwa pa nthawi ya kulumikizana kumene kunalipo ndi a Bungwe a Mpamila BMC Loyang'anira za Nkhalango. Mitengo ya zilolezozi idakhazikitsidwa poona m'mene mitengo ya kudera lakumudzi ilili komanso poona mlingo wa m'mene chuma cha m'derali chilili pa katundu wochokera m'nkhalango wokagulitsidwa kapena kukagwiritsa ntchito pakhomo ndipo yawonetsedwa ku gawo lachinayi ku ndime ya zofotokozena kumapeto kwenikweni. Ndalama zolowa pa chaka kuchokera ku misonkho ya zilolezo ndi MK1, 416,250.00 imene ndi 29.4% pamene MK3,401,500.00 00 imene ndi 70.6% ndi zochokera ku zilolezo za pakatundu wokagulitsa wochokera m'nkhalango. Zonse pamodzi zikukwana MK4, 817,750.00.

Pofuna kuonetsetsa kuti ntchito yotolera ndalama ikupitirira mpaka mtsogolo ntchito zambiri zakonzedwa kuti zidzagwiridwe ndi eni dera lachitukukoli pamodzi ndi a Bungwe a Mpamila BMC Loyang'anira za nkhalango. Amenewa adzagwira ntchitozi mosakakamizidwa. Ndalama zake zokagwirira ntchitozi zakonzedwa

moyang'ana bwino-bwino m'mene zilili ndalama zolowa
kuchokera ku zilolezo.

CHIDZIWITSO

Malipiro a ntchitozi sadzaperekedwa ndalama zenizeni
[Kashi ayi] mosinthana ndi ntchito imene yagwiridwa ayi.

GAWO LOYAMBA LA ZOFOTOKOZERA LOLEMBEDWA M'MAGOME

GOME loyamba likuonetsa ndalama zofunika kulipira
pantchito za chisamaliro cha nkhalango chaka ndi chaka

GOME 1: KALILPIRIDWE KA NTCHITO ZA KAYENDETSEDWE KA NKHALANGO

NTCHITO	CHIWERENGER O CHA	KANGA TI	Ndalam a zake	NDALAM A ZONSE
----------------	------------------------------	---------------------	--------------------------	---------------------------

	OCHITA NAWO MSONKHANO			pa tsiku	
Kutentha moyambibir a kuteteza nkhelango kuti isapsye ndi moto wolusa		15	4	200	120,000
Kuyendera Nkhelango		10	52	600	312,000
Msonkhano		15	24	200	72,000
Kusamalira mbande pa nazale		27	36	200	194,400
Kukumba dzenje		175	3	200	105,000
Kulambulir a nkhelango kuopetsa moto		175	8	200	280,000
Kuchita		3	1	2,500	7,500

kafukufuku					
wa					
malonda					
m'misika					
Kudula	13	3	1000	45,000	
timadera					
Kuika	13	3	1000	45,000	
Zizindikiro					
pa mitengo					
yosungidw					
a					
Kukolola	294	3	200	176,400	
Kupereka					
zilolezo					
TOTAL					844,400.0
					0

KULOWA NDI KUTULUKA KWA NDALAMA CHAKA NDI CHAKA

Potengera za m'magawo ena amene afotokozedwa kale, ndalama zolowa ndi zotuluka chaka chilichonse mu Buloko ya Mpamilia zawonet sedwa bwino bwino mu

gome 2 m'munsimu. Izi zionetsa kuti pansi pa chitsanzo chabwino cha kayendetsedwe kogwirizana pa chisamaliro cha zankhalango, pali chilimbikitso choti magawo onse {100%} a ndalama zotolera pa zilolezo za zinthu zokagwirira ntchito m'makomo zidzasungidwa mu thumba la ndalama la Mpamila BMC ndipo 60% mwa ndalama zotolera pa misonkho ya zinthu zokagulitsa zidzaperekedwa ku thumba la ndalama la Mpamila BMC. 30% ya ndalamazi zidzaikidwa mu thumba la chitukuko cha nkhalango [FDF] limene limasungidwa m'dziko ndi akuluakulu a zankhalango. Pamene 10% ya ndalamazi zidzaikidwa ku thumba la ndalama la Bungwe losamalira nkhalango za m'midzi pa boma [LFMB].

COME 2: CHIYEREKEZO CHA KULOWA NDI KUTULUKA KWA NDALAMA MU BULOKO YA MPAMILA

Ndalama za chisamaliro cha nkhalango mu Buloko ya Mpamila BMC	NDALAMA ZAKE	CHIWEREGERO CHA NDALAMA ZONSE PA ZANA LILILONSE[%]
Kupereka Zilolezo pa zinthu zokagwiritsa ntchito pakromo zochokera m'nkhalango	1,41,250	29.4%
Kupereka Zilolezo pa	3,401500.00	70%

zinthu zokagulitsa zochokera m'nkhalango		
Ndalama zonse zolowa	4,817,750.00	100%
Kuchotsera gawo la ndalama za kayendetsetsedwe ka ntchito zankhalango za oyang'anira bungwe lankhalango 10% ya ndalama zolowa pa katundu wogulitsa	340,150	
Zotsala	4,477,600	90%
Kuchotsera gawo la ndalama za kayendetsetsedwe ka ntchito zankhalango za bungwe la nkhalango [monga ntchito yogwiridwa, zogulidwa]	760,700	
Ndalama zokhalako pa zolowa zonse	3,716,900	

zimene zikhoza kugwira ntchito		
Chiiterekezo cha ndalama zolowa pa dera lokwanira maekala awiri ndi theka 2.5 acres[ha]	19,666.14	
Chiiterekezo cha ndalama zolowa pa banja lilionse	21,239.43	
THUMBA LA NDALAMA LA BUNGWE LOONA ZOSAMALIRA LIMODZI NKHALANGO		
Chiwerengero cha ndalama za Oyang'anira Bungwe lakumudzi loyendetsa za nkhalango[LFMB A/C]	4,817,750	
Zolowa kuchokera ku Buloko ya Mpamila pa chisamaliro cha	1,445,325	30%

nkhalango [LFMBA]		
Zotsala pa gawo la ndalama la Dipamenti ya nkhalango [30%]	3,032,275	60%

GOME 3: Kuonetsa chiwerengero cha phindu la zinthu zochoka m'timadera tating'oning'ono tam 'nkhalango chaka ndi chaka

Chiweren gero	Zinthu zochoker a m'nkhala ngo	Chiwerenge ro cholembed wa cha timadera tongoyerek ezera	Chiwereng ero cha zokolola pa hekitala imodzi[mae kala 2.5]	Chiwerenger o cha Phindu lochokera m'timadera ting'oning'ono tam 'nkhalango chaka ndi chaka
1	Ndawala	125	1125	1125

2	Nsichi	75	675	675
3	Phaso	75	675	75
4	Matabwa	125	1125	1125
5	Nkhuni	650	5850	5850

GOME 4: chithunzithunzi cha ndalama zolowa kuchokera ku misonkho ya zilolezo

Dzina la chinthu chochokera m'nkhalango	Chilolezo cha zinthu zogwiritsa ntchito pakhomo zochokera m'nkhalango	Chilolezo cha zinthu zokagulitsa zochokera m'nkhalango	ZOLOWA ZONSE [MK]
Ndawala	456,250.00	154,000.00	610,250.00
Nkhuni	910,000.00	3,240.00	4,150,000.00
Matabwa	50,000.00	127,000.00	177,000.00
ZONSE PAMODZI	1,416,250	3,521,000.00	4,760,250.00

GOME 5: Kuonetsa chiwerengero cha phindu la zinthu zokagulitsa zochokera m'nkhalango zokagulitsa

ZINTHU ZOCHOKERA MNKHALAN GO	KUFUNIKA KWAKE	KUCHULUKA KWAKE [CHIWERENGE RO CHAKE]	PHINDU /ZOTAYIKA PA NDALAMA ZOYAMBIRA NTCHITO YA MALONDA
Ndawala	8,125	9,175	1,050
Nkhuni	18,200	34,400	16,200
Matabwa	10	25	15
Total			

11. ZOFOTOKOZERA ZONSE ZIMENE ZALEMBEDWA

a. Zofotokoza mutu woyamba: **MALAMULO A
BULOKO YA MPAMILA**

b. Zofotokoza mutu Wachiwiri: **MGWIRIZANO
PACHISAMALIRO CHA NKHALANGO**

[A]MALAMULO A BULOKO YA MPAMILA

ZOLINGA ZA MALAMULO OYENDET SERA BULOKO YA MPAMILA

- 1) Kuteteza, kuyendetsa ndi kugwiritsa ntchito mosamala phindu lochokera m'nkhalango yopezeka m'dera la GVH Mpamila m'malo mwa anthu onse a Buloko ya Mpamila.
- 2) Kuika ndondomeko ya chikhazikitso cha Mamembala a bungwe la Buloko ya Mpamila

Padzayenera kukhazikitsidwa komiti ya Mamembala khumi motere:

- 1) Wapampando
- 2) Wachiwiri kwa Wapampando
- 3) Mlembi
- 4) Wachiwiri kwa Mlembi
- 5) Msungichuma
- 6) Mamembala asanu

Theka la Mamembalawa lidzakhala akazi imene ndi 50%. Padzakhalanso mamembala asanu enanso odziwa zachilengedwe amene adzathandiza kwambiri komiti yaikuluyi. Mamembala amenewa adzasankhidwa kuchokera m'midzi ya m'dera la GVH Mpamila.

ENA ONSE ZIDZAKHALA MOTERE

- Padzakhalala onse oonetsa chidwi pantchito zankhalango
- Onse okhala m'midzi pansi pa ulamuliro wa GVH Mpamila adzaikidwamonso

- Mafumu, ma Gulpu amidzi [GVH] ndi Mwinimtunda[Chalo] ndi amene adzapeleka upangiri ku komiti imeneyi zikafunikira ktero

NTCHITO ZA BUNGWE LOYENDETSZA ZANKHALANGO/AUDINDO

Ntchito ndi udindo wa komiti ya chisamaliro cha nkhalango

- Kuonetsetsa kuti phindu la ndalamu likugwiritsidwa ntchito bwino
- Kuonetsetsa kuti malamulo a gululi akutsatidwa
- Kupereka malipoti achitukuko ndi zonse zimene zakwaniritsidwa ku anthu onse a m'dera
- Kupereka malipoti achitukuko ndi zonse zimene zakwaniritsidwa kwa Gulpu, Chalo ndi Ogwira ntchito zankhalango
- Kulanda zonse zimene zatengedwa ku nkhalangoyi opanda chilolezo

NTCHITO ZA MAMEMBALA OSANKHIDWA

Wapampando ndi wachiwiri wake

Ntchito zawo

- Kuchititsa misonkhano
- Kukonza mitu ya zofunika kukakambirana ku msonkhano
- Kukonza ndondomeko ya ntchito zokachitika zokhudzana ndi ku nkhalango
- Kuonetsetsa kuti malamulo kutsatidwa

- Kukhala m'modzi wa osainira pakakhala zinthu zofunika kutapa ndalama ku banki
- Kudziwitsa okhudzidwa ena onse za m'mene ntchito ikuyendera
- Kusiyira Mamembala ena kuti akagwire ntchito m'malo mwawo akatanganidwa

Zowayenereza

- Akhale wodziwa kulemba ndi kuwerenga
 - Akhale wachidwi ndi ntchito zankhalango
 - Akhale wochokera mwa a GVH Mpamila
 - Akhale osamangidwapo
- .

MLEMBI NDI WACHIWIRI WAKE

Ntchito zawo

- Kulemba zokambirana pa nthawi ya misonkhano uliwonse[maminitsi]
- Kulemba makalata oitana anthu pakafunika misonkhano
- Kuwerenga maminitsi a mfundu zonse za msonkhano umene udachitika m'mbuyo mwa msonkhano umene ukufuna kuchitikawo
- Kukhala m'modzi wa osainira pakakhala zinthu zofunika kutapa ndalama ku banki
- Kulondoloza ndi kulinganiza zimene Msungi akulemba
- Kulemba ndi kusunga zolembedwa za katundu yense wa gululi

Zowayenereza

- Akhale wodziwa kulemba ndi kuwerenga
- Akhale osamangidwapo
- Akhale wachidwi ndi ntchito zankhalango

- Akhale wochokera mwa a GVH Mpamila

MSUNGICHUMA

Ntchito zake

- Kusunga ndalama ndi katundu wa gulu la Mamembala a Buloko ya Mpamila
- kusunga zolembedwa zonse zokhudza ndalama ndi katundu
- Kukhala m'modzi wa osainira pakakhala zinthu zofunika kutapa ndalama ku banki
- Kupereka malipoti a za chuma zonse kwa anthu onse m'derali

Zomuyenereza

- Akhale wosamangidwapo
- Akhale wodziwa masamu [kuwerengera zinthu]
- Akhale munthu wodalirika

MAMEMBALA A BUNGWE

Ntchito zawo

- Kuthetsa mikangano yobuka pakati pavo
- Kuthandiza kukonza mitu ya zofunika kukakambirana ku msonkhano
- Kuimirira Gulu lawo kukafunikira kutero

Zowayenereza

- Akhale wachidwi ndi ntchito zankhalango
- Akhale wonena mfundo zothandiza ndi zoona
- Akhale wochokera kwa GVH Mpamila

Ntchito ndi udindo wa anthu ena onse m'dera la Buloko ya Mpamila

- Kutenga gawo pa chisamaliro cha nkhalango m'dera la Mpamila
- Kutenga gawo pamene masankho akuchitika
- Ali ndi udindo wowonetsetsa kuti ali ndi ufulu wopeza phindu losiyanasiyana
- Ali ndi ufulu wothetsa komiti yoona za chisamaliro cha nkhalango kukafunikira kuteru
- Ali ndi udindo kukhalapo nthawi ya misonkhano ya ntchito zawo nthawi zonse

Zowayenereza pa udindo

- Ayenera kuti achokere kwa GVH Mpamila
- Akhale ndi chidwi ndi ntchito zankhalango

Nthawi yokhala pa udindo

- Zisankho zidzachitika zaka zitatu zilizonse
- Munthu adzasankhidwa ndi kukhala Membala motsogozana kawiri kokha.

KUCHOTSEDWA KWA A PAUDINDO [MAMEMBALA]

- Ngati satsatira malamulo okhazikitsidwa
- Ngati Membala alephera kugwira ntchito zake mu bungweli

Mphamvu zopatsidwa kwa komiti ya Mpamila

- Kuthetsa mikangano yobuka pakati pawo
- Kulanda zonse zimene zatengedwa ku nkhalangoyi opanda chilolezo
- Kulanda zida zimene zagwiritsidwa ntchito kapena zimene zikukagwira kumene ntchito yotengera phindu losiyanasiyana m'nkhalangoyi mopanda chilolezo

KUTHETSA BUNGWE

- Bungweli lidzathetsedwa pakapita zaka zitatu
- Bungweli lidzathetsedwa ngati laononga ndalamu za gululi.

UMEMBALA

- Woyenerera kukhala Membala ndi wina aliyense wochokera mwa GVH Mpamila
- Zisankho zidzayenera kuchitika mwa mtendere ndi mopanda chinyengo molumikizana ndi Chalo[Mwinimtunda]
- Aliyense wochokera m'dera la GVH Mpamila amene akukwanitsa zomuyenereza pa udindo ali ndi ufulu wopikisana nawo pampandowo
- Lamulo limene limati munthu aliyense saloledwa kuvota kawiri lizidzagwiritsidwa ntchito pa nthawi yotereyi.

Masankho adzachitika motani?

- Kwenikweni adzachitika pakapita zaka zitatu
- Aliyense wofuna kudzakhala Membala mtsogolomo adzalipira K200.00

Zifukwa zosakhalira Membala wa gululi

- Ngati munthu sachita monga mwa malamulo mwadaladala
- Akasamuka kuchoka m'dera la GVH Mpamila

UFULU WOKADANDAULA KWINA

- Membala aliyense ali ndi ufulu wokamang'ala kwa a GVH Kenaka kwa Chalo ngati sadakhutitsidwe ndi chigamulo cha Mpamila BMC

KAYENDETSEDWE KA GULULI

NTCHITO ZA ALIYENSE WA GULULI

- Kukhalapo misonkhano ikamachitika
- Kutenga gawo pa nkhanzi za nkhalango
- Kukonza ndondomeko za ntchito zankhalango ndi anthu ena onse

Nthawi yokumanirana kuchita misonkhano

- Mpamila BMC idzayenera kukumana kamodzi pa mwezi
- Mpamila BMC idzayenera kuchititsa msonkhano ndi anthu a m'derali kamodzi

KUCHULUKA KWA OYENEREZEDWA KUYAMBA MSONKHANO ATAFIKA PA MALO OSONKHANA

- Ayenera kukwanira theka la Mamembala a bungwe loyendetsa ntchito za gululi.

- Oimirira mudzi uliwonse apabungwe lalikulu ayenera kukhalapo pamene Mpamila BMC ikukumana ndi anthu [Nawonso anthu ayenera kukwanira theka la chiwerengero cha anthu onse m'derali kapena kpitirira pamenepa kuti payambike msonkhano].

KAYENDETSEDWE KA NDALAMA

- A bungwe la Mpamila BMC ayenera kutsekula buku la ku banki
- Msungichuma azidzalandira ndalama ndi Kupereka malisiti ake, azidzalemba zonse zokhudza ndalama zolowa ndi zotuluka pa ntchito zonse za Buloko ya Mpamila m'mabuku ake mwa ndondomeko yake.
- Ndalama zonse zolipira zidzayenera kuvomerezewa zisanatulutsidwe poonetsetsa kuti makalata ake onse olipirira akusainiridwa ndi kuvomerezewa.
- Ndalama zonse zotolera zidzagwira ntchito izi
 - Kubwereketsa kwa ofuna ngongole zazing'onozing'ono [20%]
 - Kuthandiza nthawi ya maliro [20%]
 - Kuthandiza osowa, amasiye, okalamba ndi opezeka ndi HIV ndi AIDS [20%]
 - Kuyendetsa ntchito za Buloko ya Mpamila [40%]

- c) Kubweretsa chiongola dzanja mu dongosolo la kubwereketsa ngongole zazing'onozing'ono [20%]

MFUNDO ZOFUNIKA KUTSATA PAKATI PA AMAYI NDI ABAMBO PAKUSASIYANA KWAO PAMAUDINDO AWO

- Osatengera kuti ndi wamkazi kapena wamwamuna aliyense adzayenera kutengapo gawo pa ntchito zosiyanasiyana kupatula okhawo amene ndi olumala, odwala, ndi okalamba.
- Phindu lochokera mu Buloko ya Mpamila komanso zonse zofunika kusonkherana poyendetsa ntchito za m'nkhalango zidzayenera kugawidwa mofanana pakati pa mamembala onse.

NDONDOMEKO YA NTCHITO YOSUNGA ZOLEMBEDWA ZONSE ZOKHUDZA NDALAMA ZOLOWA NDI ZOTULUKA

Bungwe loyendetsa za nkhalango lidzayenera kukhala ndi mabuku awa

- a) Buku lolembamo mfundu za msonkhano uliwonse [Miniti buku]
- b) Buku la Zolowa
- c) Buku la Zilolezo

- d) Buku la maulendo oyendera nkhalango
- e) Buku lolembamo m'ndandanda wa zofunika zina monga katundu ndi maina a anthu [Register]
- f) Buku la milandu ndi Zilango

KUKONZEDWA KWA MALAMULO A BUNGWEI

Kukonzanso malamulo kudzachitika zaka ziwiri zili zonse kudzera m'njira ziwiri . Yoyamba ndi pamene anthu akhoza kuchita kupempha kwa a bungwe ndipo yachiwiri ndi pamene a bungwe akhoza kuchita kupempha kwa anthu onse kuti pakhale kusintha koteroko.

KUGAWANA PHINDU LA M'NKHALANGO

Phindu limene lilipo likuphatikizapo ndalama ndi zina zonse zochokera m'nkhalango. Izi zidzayenera kugawidwa mofanana ndipo membala aliyense ndi woyenera kulandira nawo zimenezi. Odzaongolera zonsezi ndi a Bungwe la BMC ndi kuvomerezewa ndi anthu onse a m'derali.

KUYAMBA KUGWIRA NTCHITO KWA MALAMULO ANG'ONO A BULOKOYI

Malamulo a Mpamila pamodzi ndi malamulo ongokonzedwa kumene adzayamba kugwira ntchito onse ofunika kuvomereza akasainira.

OSAYINIRA ONSE

Wosainira

Tsiku

.....
.....
Wapambando wa Buloko ya Mpanang'ombe

.....
.....
GVH [Ogulupu]

.....
.....
Mwinimtunda /Chalo [T/A]

.....
.....
Bwanamkubwa wa Boma lonse [DC]

ZOFOTOKOZERA MUTU WACHIWIRI:

MGWIRIZANO PACHISAMALIRO CHA NKHALANGO PAKATI PA BOMA NDI ANTHU

12. MGWIRIZANO WOYENDETSA LIMODZI NTCHITO ZACHISAMALIRO CHANKHALANGO

[Lamulo la zankhalango, la 1997, Gawo 25]

Pangano lino lakonzedwa tsiku la lero [REDACTED]
pa..... mwezi
wa..... Pakati
pa Wamkulu wowongolera Zankhalango, miyala ndi migodi
M' Malawi, amene akuimirira Boma la Malawi ndi nzika zonse
zokhala m'dera la mudzi/midzi [REDACTED]
iyi.....
...ya [REDACTED]
Mwinimtunda[T/A]..... bo
ma la kuimiriridwa ndi [REDACTED]
..... m'malo
mwa Bungwe la kumudzi loona zankhalango[limene muno
likutchedwa kuti LFO] komanso lodziwika ndi Dzina la Bungwe
La Chigawo Chachikulu Losamalira za Nkhalango [BMC]. Pano
Boma lifuna kupanga mgwirizano ndi LFO kupereka mwayi
woyendetsera limodzi ntchito zankhalango molumikizana ndi
Maofesi a Boma oona za nkhalango [Forestry Dept.] pa zinthu
zonse zofunikira zochokera mu Buloko ya [REDACTED]
.....
..... nkhalango yosungidwa ya [REDACTED]

.....ndi cholinga chopititsa patsogolo chisamaliro cha nkhalango chosalekeza komanso kulimbikitsa kupititsa patsogolo miyoyo ya anthu okhala m'madera oyandikana.

Mu Mgirizano uno zimene tagwirizana ndi izi:

1. Pakukhutitsidwa ndi dongosolo la m'mene likuyendetsera ntchito Bungwe la kumudzi loona zankhalango[LFO], Boma la Malawi lidzavomereza ndi kupereka mphamvu ku bungweli kuti liteteze, lisamalire ndi kuongolera kayendetsedwe kabwino ka nkhalango mosaonongeratu koma mosungako mathandizo ena a mawa kuchitira ubwino aliyense wa m'dera lam'mudzi wa.....
2. Bungwe la kumudzi loona zankhalango lidzavomereza ndi kukhala ndi udindo woteteza, kuyendetsa, kuongolera ndi kugwiritsa ntchito bwino zinthu zochokera m'nkhalango mosaonongeratu koma mosungako mathandizo ena a mawa monga mwa malamulo ndi mfundu zimene zokhazikitsidwa mu mgwirizano lino komanso mu ndondomeko ya chikonzero cha mgwirizano pakasamalidwe ka nkhalango imene yayikidwa pamapeto pa chikonzerochi.

UDINDO WA BUNGWE WA LAKUMUDZI LOONA ZA NKHALANGO

3. Mwa paderadera Boma la Malawi likuperekwa mphamvu ku Bungwe la kumudzi loona zankhalango[LFO] ngati izi zitatsatidwa motere:

- a) Ngati nkhalango idzasungidwa ndi kusamalidwa monga mwa njira zovomerezeka za chisamaliro cha nkhalango zimene zaikidwa mu ndondomeko ya chikonzero cha mgwirizano pa kasamalidwe ka nkhalango pamapeto pa chikonzerochi.
- b)** Bungwe la kumudzi loona zankhalango lidzaonetsetsa kuti mphamvu zimene linalandira kuchokera ku Boma la Malawi mu malamulo a zankhalango a m'chaka cha 2001 ndi ena otsatira zikugwira monga mwa mgwirizano woilembetsa Bungwe la kumudzi loona zankhalango.
- c)** Bungwe la kumudzi loona za nkhalango [LFO] lidzateteza, lidzayendetsa, lidzaongolera ndi kugwiritsa ntchito bwino mathandizo osiyanasiyana a m'nkhalango m'njira ya chisamaliro chosungako zina molingana ndi mphamvu zimene adapatsidwa. Bungweli lidzaperekanso zilolezo ndi ziphaso za zinthu zonse zochokera m'nkhalango zimene kwenikweni zimathandiza anthu m'madera awo komanso pa nthawi yokolola zambiri pamene afuna kukagulitsa monga m'mene zafotokozeredwa mu chikonzero cha chisamaliro cha nkhalango
- d) Pothandiza Wamkulu woona zankhalango pa boma[DFO], Bungwe la kumudzi loona zankhalango[LFO] lidzaperekwa makalata ochitira umboni [makalata osonyeza

umwini wa chinthu], kuvomereza kumene munthu wakatenga zochokera m'nkhalango ndi umwini wa katundu amene ali kuyang'aniridwa ndi bungweli. Bungweli likhoza kuthandizanso aliyense wofuna kalata ya umboni ngati ali ndi zinthu zofuna kugulitsa zochokera ku mitengo ya m'nkhalango pakulipempha Kalata yochokera kwa Wamkulu woona zankhalango pa boma[DFO]

e) Mathandizo onse ochokera m'nkhalango adzagwiritsidwa ntchito mofanana ndi onse okhala m'derali molingana ndi ndondomeko zake za kugawana phindu lochokera mu nkhalango monga mwa chikonzero ndi malamulo a Bungwe la kumudzi loona za nkhalango [LFO].

f) Ndalamu zonse zotolera kuchokera **a** m'nkhalango zidzagawidwa mofanana ndi onse okhala m'derali molingana ndi ndondomeko zake za kugawana phindu lochokera mu nkhalango monga mwa chikonzero ndi malamulo a Bungwe la kumudzi loona za nkhalango [LFO].

g) Magawo khumi mwa magawo zana limodzi [10%] a ndalamu zotolera ku zilolezo ndi ziphaso pa phindu lobwera chifukwa chogulitsa zinthu za m'nkhalango zidzaikidwa mu buku la ku banki la oyang'anira za nkhalango ya ku mudzi laLFMB[Local Forest Management Board] ndipo izi zizidzachitika miyezi itatu ili yonse.

h) Magawo makumi atatu mwa magawo zana limodzi [30%] a ndalamu zotolera ku zilolezo ndi ziphaso pa phindu

lobwera chifukwa chogulitsa zinthu za m'nkhalango zidzaikidwa mu buku la ku banki nambala wani la Thumba la Chitukuko zinthu zochokera m'nkhalango ya ku mudzi [Forest Development Fund Account] ndipo izi zizidzachitika miyezi itatu ili yonse.

- i) Ndi choyembekezeka kuti magawo makumi asanu ndi limodzi mwa magawo zana limodzi [60%] a ndalama zotoleredwa ndi Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] zogawana zitachitika monga m'mene zafotokozedwera pamwambapa pa [g] ndi [h] 60% imeneyi idzagwiritsidwa ntchito ndi a bungweli pa chitukuko cha nkhalango, chisamaliro ndi kuyendetsera ntchito za nkhalango. Padzakhala kugwiritsa ntchito ndalamazi mkatì ndi kunja komwe kwa dera la mgwirizano woyendetsera Buloko ya Mpanang'ombe.
- j) Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] lidzaonetsetsa kuti zolembedwa zonse za ndalama ndi zilolezo zonse zimene zaperekedwa zikupezeka mosavuta akadziwitsidwa kuti akuzifuna Wamkulu wa zankhalango m'Malawi ku unduna woona za nkhalango [**Director of Forestry**] wachiwiri wake kapena Bwanamkubwa [DC] atauzidwa ndi Wamkulu wa zankhalango m'Malawi kapena Bwanamkubwa [DC].
- k) Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] lidzaimirira anthu onse a m'dera lake ndi kukhala ndi udindo woyankha china chilichonse chimene anthuwo angafunse

pa ntchito yake m'deramo ndipo bungweli lidzayendetsanso ntchito zakezo monga mwa malamulo okhazikitsidwa a zankhalango amene adavomerezedwa.

UDINDO WA DIPATIMENTI YOONA ZA NKHALANGO

4. Mwapaderadera wamkulu woona zankhalango pa boma[DFO] ndi onse omuimirira pantchito yake adzayenera

a) Kupereka maluso a ntchito yawo ndi kulimbikitsa ntchito yokwaniritsira zolina zosamalira nkhalango limodzi ndi Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] ndi kuunikanso mu nthawi yabwino ndondomeko ya chikonzero cha mgwirizano pakasamalidwe ka nkhalango yoikidwa kumapeto kwa zonsezi.

b) Kulangiza ndi kuthandiza m'njira zosiyanasiyana pochita kalondolondo pa kayendetsedwe ka ndalamza nkhalango kuphatikizapo kuchititsa misonkhano, zisankho zazikulu ndi zazing'onozing'ono, kusunga zolembedwa zonse za pamisonkhano, kulongosola kayendetsedwe ndi chisamaliro cha katundu ndi ndalamza Buloko ya Mpanang'ombe komanso kulemba malipoti.

c) Kupereka zinthu zosiyanasiyana zofunikira kuyendetsera ofesi ya Bungwe la kumudzi loona zankhalango[LFO] {utangovomerezedwa mgwirizano unowu pa kusainira} monga mabuku a ndalamza zolowa

ndi kutuluka m'thumba la ndalama [**cash books**], mabuku olembamo zonse zogwirizana pa misonkhano [**Minute books**], makalata a zilolezo amene amakhala awiriawiri, mapepala olembapo Kalata za ofesi amene amakhala oikiratu keyala [adiresi], chidindo cha ofesi ya Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] kapena chizindikiro china chapaderadera cha ofesiyi ndi zinthu zina zofunikira ndi cholinga cholimbikitsa kuchita zinthu mosabisa ndi kulembera zonse za chisamaliro ndi kayendetsedwe koyenera ka zinthu za nkhalango komanso kukhazikitsa dongosolo labwino la kaperekedwe ka ziphaso pa katundu wochokera m'nkhalango. Zikuyembekezezeka kuti bungweli lidzachita ntchito yokagula katundu ameneyu pokhapokha kutolera ndalama kutachitika.

- d) Kuthandiza kulumikizana pantchito zolimbikitsa malamulo a zankhalango kumene kumakhalapo pakati pa Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO], mafumu, anthu eni dera, magulu olimbikitsa bata poyendera m'dera, ogwira ntchito m'boma a zachitetezo ku madera, wamkulu woweruza milandu pa boma motsata ndondomeko ya chikonzero cha mgwirizano pakasamalidwe ka nkhalango imene yaikidwa kumapeto kwa zonsezi.
- e) Kuyendera limodzi ndi Bungwe la kumudzi loona zankhalango [LFO] malire a Buloko amene adalembedwa mu ndondomeko ya chikonzero cha

mgwirizano wosamalira zachilengedwe m'nkhalango kuti chisamaliro chikhale monga m'mene zilili mu mgwirizano uno komanso monga m'mene zilili poona mlingo ndi mfundo za ndondomeko yakutengako gawo pa ntchito zankhalango muno m'Malawi.

- f) Kugwira ntchito limodzi pomasainira zilolezo ndi ziphaso za katundu wochokera m'nkhalango kusonyeza kuvomereza ntchito imene yachitika ya katundu wokagulitsidwa kapena kukagwiritsira ntchito ya m'makomo ngati munthuyo waguladi potsatira ndondomeko ya m'chikonzero chimene chilipo cha mgwirizano pakasamalidwe ka zachilengedwe za m'nkhalango.
- g) Kupereka makalata ochitira umboni polinganiza ndi makalata otsimikizira pa katundu amene adatulutsidwa kuchokera m'nkhalango motsatira ndondomeko yokhazikitsidwa popereka ziphaso kuti pakhale kutulutsa katundu wochokera m'nkhalango movomerezeka.
- h) Kupereka matandizo osiyanasiyana ku Bungwe la kumudzi loona za nkhalango[LFO] mogwirizana ndi Ogwira ntchito za chisamaliro cha zachilengedwe, malangizo okhudza za milandu pa katundu wochokera m'nkhalango, kuthandiza pa kayendetsedwe ka bungwe ndi kagulitsidwe ka zinthu zachilengedwe za m'nkhalango monga m'mene kufunikira.

- i) Kupangitsa misonkhano yophunzitsa anthu kwa masiku angapo kuti adziwe ndi kupititsa patsogolo maluso osiyanasiyana pa kayendetsedwe ka bungwe, maluso a zamanja, ndi kuthekera kwawo pa kayendetsedwe ka bungwe loyang'anira bungwe loyendetsa za nkhalango ya kumudzi [LFO], kupititsa patsogolo kuthekera kwawo ma Chalo [T/A] ndi Mamembala ena a m'derali.
- j) Kuvomereza ndi kulimbikitsa kuti pakhale chiterezo ndi njira zobweretsera bata ndi mtendere zimene mabungwe a FMB ndi LFO amatsata pamodzi ndi ena onse m'derali motsatira Lamulo la zankhalango la 1997, komanso m'ndandanda wa malamulo ang'onoang'ono ena a 2001 ndi mgwirizano wolembetsera bungwe la zankhalango ya kumudzi [LFO Registration Agreement}

CHIYAMBI, KUTALIKA KWA NTHAWI YAKE NDI KUTHA KWAKE KWA MGWIRIZANO

5. Mgwirizano uno udzayamba kugwira ntchito ukadzangovomerezewa [ukadzangosainidwa] ndi wamkulu woona zankhalango M'Malawi [Director of Forestry], Oimirira magawo osiyanasiyana a zankhalango, ndipo udzakhala ukugwira ntchito mpaka muyaya monga m'mene mfundo 6 ndi 9 zikunenera m'munsimu.

6. Wamkulu woona zankhalango m' Malawi [DO F] adzakhala nazo mphamu zothetsera mgwirizano uno ndi kuchotsa onse a m'maudindo awo ndi cholinga choteteza, kuyendetsa, kuongolera ndi kugwiritsa ntchito bwino zinthu zonse zochokera m' nkhalango pokhapokha patachitika izi :
- a) Ngati pali kutayirira kapena kulephera kuteteza, kuyendetsa, kuongolera ndi kugwiritsa ntchito bwino Buloko ya Mpanang'ombe.
- b) Ngati bungwe loyendetsa za nkhalango ya kumudzi [LFO] lopezeka litaphwanya kwakukulu mgwirizano uno.
7. Mphamu zimene zaperekedwa pa mfundu 6 pamwambapa sizoyenera kuzigwiritsa ntchito **pokhapokha** Wamkulu woona zankhalango m' Malawi [DO F] **atayesetsa kwathunthu ndi kukanika** njira **zonse** zimene akhoza kufufuza cuti athetsere mwa mtendere zovuta zimene zinalipo pa nthawiyo.
8. Pa kuchenjeza anthu a m'derali, Wamkulu woona zankhalango M' Malawi [DO F] adzayenera kunena zofooka ndi kupereka njira ndi kutalika kwa nthawi zokonzera zofookazo.
9. Bungwe loyendetsa za nkhalango ya kumudzi [LFO] likhoza kuthetsa mgwirizano uno nthawi ina ili yonse popereka chidziwitso chosachepera masabata asanu ndi atatu [8 wks] pokhapokha patachitika izi:

a) Pokhapokha ngati pali kuphwanya Kwakukulu kwa mgwirizano uno

b) Ngati anthu a m'derali ataona kuti alephera pa zifukwa zawo kapena ataona kuti sakufuna kupidiriza ntchito zokhazikitsidwa za chisamaliro cha nkhalango chochitira limodzi ndi Boma mu Buloko ya Mpanang'ombe.

10. Pamene chidziwitso chothetsera mgwirizano chaperekedwa, Bungwe loyendetsa za nkhalango ya kumudzi [LFO] lidzakhala ndi udindo wowonetsetsa kuti dera la nkhalango ndi lotetezedwa mpaka pamene bungwe losamalira nkhalango kapena Boma litatenganso udindo wake pa Buloko imeneyi.

11. Zigawo za madera okhazikitsidwa a nkhalango zidzaonetsedwa monga m'mene zilili pa mapu ongolemba pamanja amene amapanga nawo gawo la Chikonzero cha kasamalidwe ka zankhalango zimene zafotokozedwa mu mgwirizano uno wa chisamaliro cha nkhalango woyendetsera limodzi ndi Boma

NTCHITO YOLEMBA NDI KUIKA MALIRE

MIKANGANO

12. Pamene mkangano wa zankhalango ubuka mgwirizano uno ulipo, nkhani yotere idzaprekedwa kwa anduna a za

nkhalango amene ali woyenera kuweruza ndi kuthana ndi zoterezi. Koma ngati wina sakhetitsidwa ndi chigamulo cha andunawa, ali ndi ufulu wokamang'ala ku bwalo lina lalikulu [la High Court].

13. Ovomereza[Osainira]

.....
Tsiku.....
Wamkulu wa Zankhalango [DOF]

.....
Tsiku.....
Wapampando wa Bungwe la kumudzi la zankhalango [LFO]
.

.....Tsiku.....
.....
OCHITIRA UMBONI [MBONI ZAKE]

.....Tsiku.....

A mfumu a m'mudzi [a Nyakwawa [VH]

.....Tsiku.....

Mwinimtunda/Gogo/Chalo [T/A]

.....Tsiku.....

Bwanamkubwa wa Boma lonse [DC]

POTHERA!

MANKHUE BLOCK MANAGEMENT PLAN (NTCHISI)

13. SIGNED:



DIRECTOR OF FORESTRY
2013-04-10
P.O. BOX 30048
LILONGWE 3
DIRECTOR OF FORESTRY TEL.: 01 771 000
Dated.....10-04-13

AND




G. Ngwira

CHAIRPERSON, LOCAL FOREST ORGANISATION

Dated.....24/05/2013.....

WITNESSES:



Mr. Chirwa

VILLAGE HEADMAN/WOMAN

Dated.....24/05/2013



FRK & D. S.

TRADITIONAL AUTHORITY

Dated.....24/05/2013

CHIEF NTHONDO MTSIRO HEADQUARTERS	24 MAY 2013
 _____ Chief NTHONDO MTSIRO HEADQUARTERS	

DISTRICT COMMISSIONER

Dated.....24/05/2013

THE DISTRICT COMMISSIONER	27 MAY 2013
	P.O. BOX 1, NTCHISI